
# BUKHU LOTHANDIZIRA KULONDOLOZA NTCHITO ZAMIGODI



OXFAM

cepa

Centre for Environmental Policy and Advocacy



# ZAMKATIMU



Mbiri ya ntchito ya kafukufuku wa miyala pa phiri la Nzongwe........................................ 3
Kutenga udindo wa zisankho, ziganizo, ntchito ndi zotsatira zake (accountability)...... 3
Zolinga za ndondomeko yotsogolera kawuniwuni............................................................ 3
Zoyenera kuti anthu awunikire ndi kulondola................................................................ 5
Mfundo yoyamba: Kusamalira zachilengedwe.................................................................. 5
Mfundo yachiwiri: Kusamalira zoipa zochokera kuntchito ya mgodi............................. 5
Mfundo yachitatu: Mgwirizano wa makampane ndi anthu a kumudzi pa chitukuko kumadera okhuzidwa ndi mgodi................................................................ 9
Mfundo yachinayi: Kumva maganizo a anthu pa chitukuko cha mgodi chisanayambike.......................................................................................................... 11
Mfundo yachisanu: Kupewa ngozi ndi kuteteza umoyo wa anthu................................... 11
Umboni wa zolembedwazi................................................................................................ 12


**Zotsatira za ntchito za migodi.** Chithunzi chinatengedwa ndi CEPA.

# BUKHU LOTHANDIZIRA

Kulondoloza ntchito zamigodi

Centre for Environmental Policy and Advocacy




Chinthunzichi chatengedwa kuchokera pa:
http://www.mkango.ca/s/songwe.asp

# MBIRI YA NTCHITO YA KAFUKUFUKU WA MIYALA PA PHIRI LA NZONGWE




Boma la Malawi linapeleka chilolezo kukampani ya Mkango Mineral Resources yochokera mdziko la Canada kuti idzafufuze ngatidi nthaka ya ku Mauzi T/A Nazombe phiri la Nzongwe ikusungira miyala yofunikira pantchito zopanga matelefoni, mabatile komanso makina a kompyuta mwa zina. Potsatira izi kampani ya Mkango yakhala ikufufuza miyalayi kuyambira chaka cha 2011 pomwe inalandira chilolezo chofufuzira miyalayo chomwe chikuyenera kutha mchaka cha 2017. Ntchito zina zomwe zikupitilira ndi ntchito yoyeza fumbi, mpweya komanso madzi m'madera ozungulira malo omwe ntchito yamigodi ingadzagwirike. Chiyembekezo ndichoti kampani ya Mkango itha kudzayamba ntchito zake zamigodi kudera la Mauzi mchaka cha 2020 ngati boma lingadzapeleke chilolezo kukampaniyi chokumbira miyalayi mdziko muno ntchito ndi zotsatira zakafukufuku wake zikatha bwino.

Ena mwa magulu omwe akhala akugwira ntchito zamigodi kwa T/A Nazombe ndi monga Ufulu Wathu, Community Action Group, Reflection Action Cycles ndi magulu ena a achimyamata. Pakadali pano magulu onsewa akugwira ntchito limodzi pansi pa ntchito yomwe bungwe la CEPA ikugwira ndi chithandizo chochokera ku OXFAM. Ntchitoyi ndiyofuna kuwonetsetsa kuti amayi, abambo komanso achinyamata akutengapo gawo komanso kupeza mwayi ofanana paphindu limene likuchokera kuntchito zamigodi. Ntchitoyi ndiyolimbikitsa anthu akuderaku kuti adzitha kufufuza ndi kulondoloza momwe ntchito zamigodi zikuyendera mdera lawo kuti ziwapindulire.

#### KUTENGA UDINDO WAZISANKHO, ZIGANIZO, NTCHITO NDI ZOTSATIRA ZAKE (ACCOUNTABILITY)

Mawu amenewa amawunikira udindo omwe kampani, boma, magulu kapena anthu ali nawo povomeleza ziganizo zawo, kusabisa, kusakhotetsa chilungamo kapena kusunga mfundo zofunikira pakagwiridwe kawo kantchito zosiyanasiyana kuphatikizapo ntchito zamigodi.

#### ZOLINGA ZA NDONDOMEKO YOTSOGOLERA KAWUNIWUNI

Kuthandiza anthu akumudzi kuchita kawuniwuni ndi kalondolondo wamomwe kampani yamigodi ikugwilira ntchito yake yofufuza miyala kapena kukumba kumene. Choncho, anthu akudera ayenela;

- Kuwonetsetsa kuti upangiri wokhudzana ndi ntchito zamigodi wapelekedwa kwa anthu akudera kuti adzitha kutsatira bwino zonse zomwe zikuchitika kudera kwawo kuti nawo apindule, ndi;
- Anthu akumudzi akhale ndikuthekera kokambirana ndi kampani, boma kapena magulu okhudzidwa ngati pali zolakwika pakagwiridwe kantchito yokhudzana ndi migodi mdera mwawo.



**Mpoto Lagoon amapezeka ndi zachilengedwe zochuluka amalandira madzi kuchokera kuphiri la Nzongwe:** Chithunzi chinatengedwa ndi a CEPA.

# ZOYENERA KUTI ANTHU AWUNIKIRE NDI KULONDOLA



## MFUNDO YOYAMBA: KUSAMALIRA ZACHILENGEDWE

Anthu akumudzi ndi magulu onse okhudzidwa ndichitukuko komanso umoyo wa anthu ali ndi udindo owonetsetsa kuti kampani yamigodi komanso boma akupeleka uthenga wolondola pa mmene ntchito zamgodi pofufuza kapena kukumba miyala zikhudzira chilengedwe monga nkhalango, madzi, mtsinje, nthaka ndi zachilengedwe zina, ndi kusamala kwake.

1. Anthu akuyenera kudziwa zinthu zotsatilazi;

   i. Kudziwa ngati kampani inachita kafukufuku wamomwe zachilengedwe komanso moyo ndi chikhalidwe cha anthu kudelako chidzakhudzidwire ndi ntchito zamgodi (Environmental and Social Impact Assessment).

   ii. Momwe kampani ikusamalira ndi kutayira zoipa zochokera kuntchito ya mgodi powonetsetsa kuti anthu, madzi komanso zachilengedwe zozungulira ndizotetezedwa.

   iii. Ntchito yobwezeletsa chilengedwe pamalo omwe ntchito yagwirika kale komanso ntchito yokwilira maenje omwe akumbidwa pofuna miyala.

   iv. Kudziwa momwe kampani ikuchepetsera chiwopyezo chakuwonongeka kwa madzi apansi, mmitsinje, mmadambo komanso malo onse omwe amasunga madzi.

Kodi angachite bwanji kawuniwuni;

   i. Anthu afufuze zolakwika kapena ziopyezo zilizonse zomwe zakhudza umoyo wawo, zachilengedwe zina monga madzi, nthaka, mpweya, ndi ziophyezo zina.

   ii. Anthu afufuze ngati kubwera kwa ntchito yamigodi kwadzetsa mavuto aliwonse ku umoyo wawo kumbali ya matenda.

**Chiwonetsero chamomwe angachitire kafukufukuyu kuti anthu amvetsetse bwino (Role Play)**

## MFUNDO YACHIWIRI: KUSAMALA ZOIPA ZOCHOKERA KUNTCHITO YA MGODI

Kampani yamigodi ikuyenera kuwonetsetsa kuti ikugwiritsa ntchito mfundo ndi ndondomeko zabwino zosamalilira ndi kutayira zoipa zomwe zimapezeka ntchito yakafukufuku kapena yokumba miyala ikamagwiridwa kudera. Cholinga ndichoti umoyo wa anthu komanso zachilengedwe zozungulira zitetezedwe kuzoyipa zomwe zikuchokera kuntchitoyi. Kampani ikuyembekezeledwa kugwiritsa, kusamalira ndi kusunga bwino zinthu zoipazi komanso kukazitaya malo oyenera omwe sangapeleke chiophyezo kumadzi, mitsinje, Nyanja, zitsime, zomera zina ndi zina, mpweya, nyama zakutchire, ziweto komanso kumoyo wa anthu ozungulira.

Makampani omwe akufuna kugwira ntchito yamigodi akuyenera kusonyeza ndikutsimikiza kuti adzachita izi:



**Unduna wa za migodi kuyendera mgodi wa Nkhachira ku Karonga:**
**Chithunzi chinatengedwa ndi a CEPA.**

# ZOYENERA KUTI ANTHU AWUNIKIRE NDI KULONDOLA



i. Adzayesetsa kupewa kuwononga dera lomwe akugwirako ntchito
ii. Adzasamalira bwino zoipa zomwe zapezeka pogwira ntchito yawo
iii. Adzateteza zachilengedwe zosiyanasiyana zopezeka kuderako akamagwira ntchito zawo
iv. Adzayesetsa kukonzanso ndikubwezeretsa chilengedwe pamalo amene awonongedwa chifukwa cha ntchito zawo zamigodi
v. Adzayesetsa kuchepetsa zotsatira zoipa zomwe zingawononge malo onse osunga madzi (mitsinje, madambo, zitsime, Nyanja ndi malo ena kuderako.

### 1. Zoyenera kuwunika

I. Anthu akuderako akuyenera kuwunikira malonjezano amene kampani inalonjeza isanayambe ntchito kuti idzatsatira posamalira ndi kutaya zoyipa zochokera kuntchito yawo yamigodi
II. Kuyendera malo omwe kampani yakhazikitsa komwe zoyipa zonse zikusungidwa kapena kutayidwa
III. Kuyendera malo onse omwe angakhale pachiwophyezo chifukwa cha zoyipa zochokera kumigodi


### 2. Choyenera Kuchita

Anthu akapeza zotsatira zolakwika pankhani yakasamilidwe ndi katayidwe kazoyipa zochokera kuntchito yamgodi akuyenera kukumana ndi magulu okhudzidwa ndi kuphwanyidwa kwa ufulu wa anthu komanso malonjezano omwe kampani inalonjeza kutsatira kuti iteteze umoyo komanso zachilengedwe zozungulira kudera pogwira ntchito zake.

### 3. Chiwonetsero chamomwe angachitire kalondolondoyu kuti anthu amvetsetse bwino



**Mankhwala owopsya ayenera kugwiritsidwa ntchito mosamala pa mgodi.**
**Chithunzi chinatengedwa kuchokera pa intaneti.**



**Madzi abwino ndi chimodzi mwa zitukuko zimene kampani ya Mkango yapeleka ku midzi ina yozungulira phiri la Nzongwe:** Chithunzi chinatengedwa ndi a CEPA.

# ZOYENERA KUTI ANTHU AWUNIKIRE NDI KULONDOLA



## MFUNDO YACHITATU: MGWIRIZANO WA KAMPANI NDI ANTHU A KUMUDZI PA CHITUKUKO KU MADELA OKHUDZIDWA NDI MGODI

Makampani ambiri akulimbikitsa kuti pazikhala mgwirizano pakati pamakampani ndi anthu akudera pankhani za chitukuko zimene makampani angapeleke kudera. Izi zilichonchi chifukwa choti makampani akuchoka ku khalidwe lopeleka thandizo kapena chitukuko kudera mwachifundo ndi kuganiza kwawo pofuna kupeleka mwayi kwa anthu akudera kuti akhale pamgwirizano wantchito zachitukuko zomwe anthu angazifune kudera kwawo. Izi zakhala zikuchitika maka pofuna Kutukula miyoyo ya anthu akudera mwachifundo. Zitukuko zochita mwachifundozi zimapangidwanso pofuna kuti amakampani adzithandize pokhala bwino ndi anthu akudera uku nawo akupindula ndi miyala yamtengo wapataliyi.



Ntchito zachifundo zimathandiza makampani kuti achite ntchito zina mowonjezera pazomwe amayenera kuchita makamaka pothandizaponso pamavuto amene angabwele chifukwa chowononga zachilengedwe kudera komwe ntchito ikugwirika. Ndi ntchito ya makampani kufufuza momwe ntchito zawo zikukhudzira umoyo wa anthu kudera komanso kutenga udindo pazachilengedwe zomwe zawonongeka chifukwa cha ntchito zawo. Iyi ndi njira imodzi yabwino yolimbikitsira ubale pakati pakampani ndi anthu okhala kuderako.

### KULONDOLA NKHANI

Motero akudera ayenela ;

i. Kukambilana ndi makampani kuti ndondomeko zoyenera zayikidwa zothandiza chitukuko kudera lomwe migodiyi ikuchitika;
ii. Kuwonesetsa kuti afikilidwa ndipo apeleka maganizo awo pofufuza zomwe akudera akufuna asanayambe kuchita ntchito zachitukuko. Izi zitha kubweletsa umodzi komanso Kutukula kagwilidwe ka ntchito makamaka pochita zinthu poyera.;
iii. Kuwonetsetsa kuti chitukuko chilichonse chapasidwa nthawi yake yozapangikila ndipo zatsindikizika kuti anthu akudera athe kulondoloza bwino;
iv. Kugwila ntchito ndiadindo akudera maka amma komiti osiyanasiyana kuti athe kulondoloza bwino.

**Chiwonetsero chamomwe angachitire kafukufukuyu kuti anthu amvetsetse bwino (Role Play)**



**Anthu akumudzi akuyenera kufunsidwa maganizo awo pamomwe chitukuko chilichonse chingagwiridwire kudera kwawo:** Chithunzi chinatengedwa ndi a CEPA.

# ZOYENERA KUTI ANTHU AWUNIKIRE NDI KULONDOLA



## MFUNDO YACHINAYI: KUMVA MAGANIZO A ANTHU PA CHITUKUKO CHA MGODI CHISANAYAMBIKE

Mfundoyi imalimbikitsa kuti anthu opezeka kudera komwe ntchito iliyonse yachitukuko mwachitsanzo yamigodi akuyenera kuchitika ayenera kufunsidwa maganizo awo komanso kutengapo mbali pamomwe ntchito zopindulira umoyo wawo zingagwiridwire. Izi zikuyenera kuchitika ntchito iliyonse asanayambike kuderako pa malo amakolo awo ndicholinga chowapatsa mwayi opeleka maganizo awo pazamomwe ntchito yachitukuko ingayendere.

i. Kuwuzidwa chitukuko chisanayambe kutanthawuza kuti anthu akudera alandile uthenga woyenela pankhani zachitukuko. Uthengawu utha kukhala okhudzana ndi chitukuko chomwe chitabwele kudera maka mfundo zokhudzana ndi mmene chitukukocho chidzakhalire, kukula kwake, chifukwa chomwe chitukukocho chabwela kudera kwawo ndi nthawi yoti anthu akudera ayembekezele kuti chitukukocho chikhalire;

ii. Ndi ntchito ya boma kuwonesetsa kuti anthu awuzidwa chitukuko chisanayambe;

iii. Kupanda kuwawuza anthu akudera zachitukuko chomwe chibwele kudera kwao, anthuwa akudera sangakhale omasuka potengapo mbali pachitukukochi.

## MFUNDO YACHISANU: KUPEWA NGOZI NDI KUTETEZA UMOYO WA ANTHU

Izi ndi ndondomeko komanso zikonzero zothandizila kupewa matenda, ngozi komanso kuvulala kwa anthu ogwira ntchito kapena anthu opezeka m'malo ozungulira mgodi. Anthu akudera ayenera kuwonetsetsa kuti moyo wawo, nthanzi lawo komanso dera lawo lidzakhala lotetezedwa ntchito zamigodi zisanayambike.

### ZOYENELA KUWUNIKA:

i. Makampani ayenela kunena poyela kwa anthu akudera mfundo zomwe iwo akugwilira ntchito maka pankhani za umoyo ndi Chitetezo pothandiza kulimbikitsa anthu akudera;

ii. Ayenera kugwira ntchito zawo powonetsetsa kuti akutsata malamulo komanso ndondomeko za boma zokhudza nkhani za umoyo ndi Chitetezo;

iii. Kampani iyenela kufotokozera anthu antchito komanso akudera za umoyo ndi chitetezo chawo kwa nthawi ndi nthawi muchiyankhulo chomwe anthu akudera amachimva bwino.

## UMBONI WA ZOLEMBEDWAZI

Bovens, M. (2007): Analyzing and Assessing Accountability: A Conceptual Framework. European Journal of Law, 13(4), 447-468.

Economic Commission for Africa (2002): Managing Mineral Wealth; Training Materials on "Management of Mineral Wealth and the Role of Mineral Wealth in Socio-economic Development". Addis Ababa, Ethiopia.

GOM, Environment Management Act 1996

GOM, Mines and Minerals Act 1981

José Antonio Ocampo, A Post-2015 Monitoring and Accountability Framework; Department of Economic & Social Affairs, CDP Background Paper No. 27 ST/ESA/2015/ CDP/27, August 2015

Mulgan, R. (2003). Holding Power to Account. New York: Palgrave.

Oxfam Malawi October 2016: Future Mining Revenues for Malawi? A Case Study of Mkango's Songwe Hill Project,

The Principles and Guidance Notes of e3 plus: A Framework for Responsible Exploration 2014

The Universal Declaration of Human Rights (1948), UN General Assembly

http://www.businessdictionary.com/definition/ accountability.html (accessed 06 December, 2016)

http://www.mkango.ca/s/songwe.asp (accessed on 07th December, 2016)

www.ifc.org/performancestandards



**Ogwira ntchito ku kampani ya mkango kuvala zozitetezela pogwira ntchito:**
**Chithunzichi chatengedwa kucrhokera mu OXFAM mining revenue report for Malawi 2016**



Kabukuka kanalembedwa ndi:
Centre for Environmental Policy and Advocacy (CEPA)
P.o Box 1057, Blantyre, Malawi
Tel: +265 212 700 104
Email: cepa@cepa.org.mw.
Website: www.cepa.org.mw